## PHUNZIRO LA 35

1. Kodi Mulungu analemba pati malamulo ake khumi aja?
-Pa mapale aŵiri a miyala.

2. Pamene Mulungu anamupatsa Mose malamulo khumi aja, Mulungu anamulamulanso Mose kuti amumangire Iye chinthu china chake. Kodi chinali chiyani?
-Mulungu anamulamula Mose kuti amumangire Mulunguyo Malo opatulika.

3. Kodi Mulungu amasoŵa nyumba yakuti adzikhalamo?
-Iyayi.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu samasoŵa nyumba yakuti adzikhalamo?
-Chifukwa chakuti Mulungu ndi mzimu.
-Chifukwa chakuti Mulungu amakhala paliponse pa nthaŵi zonse.

5. Kodi Mulungu anapereka lonjezo lotani kwa a Isirayeli?
-Mulungu analonjeza zakuti aŵadalitsa a Isirayeli akaŵamvera malamulo ake onse, koma ngati saŵamvera malamulo ake onse, Mulungu aŵapatsa chilango.

6. Kodi a Isirayeli anakatha kuŵamvera malamulo onse a Mulungu?
-Iyayi.

7. Kodi Mulungu anadziŵa zakuti a Isirayeli satha kuŵamvera malamulo ake onse?
-Inde.

8. Kodi chilango cha anthu amene akuphwanya lamulo ngakhale limodzi la Mulungu ndi chotani?
-Imfa mnyanja ya moto wosatha.

9. Kodi njira imene anapereka Mulungu kwa a Isirayeli kuti apulumuke inali yotani?
-A Isirayeli akachita tchimo ndi kuphwanya limodzi mwa malamulo a Mulungu aja, a Isirayeliwo ankapita ku malo opatulika aja atatenga magazi a nyama.

10. Kodi Mulungu ankachita chiyani akawona magazi a nyamawo?
-Mulungu akawona magazi a nyamawo, ankadikira kaye osapereka msanga chilango kwa a Isirayeli mpaka chilango choyenera pa tchimolo chitachitika.

11. Kodi Mulungu ankafuna kuti Mose ndi a Isirayeli amange bwanji malo opatulikawo?
-Ngati m'mene anamulamulilira Mulungu.

12. Kodi mayina a zipinda ziŵiri zimene Mulungu anamulamula Mose kuti akapange m'malo opatulika aja ndi ati?
-Chipinda choyamba chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulika.
-Chipinda chachiŵiri chinkatchedwa kuti Chipinda Chopatulikitsitsa

13. Kodi dzina la bokosi limene Mulungu anamulamula Mose kuti apange ndi kuliyika M'chipinda Chopatulikitsitsacho linali chiyani?
-Bokosilo linkatchedwa kuti Likasa la Chipangano.

14. Kodi tanthawuzo la nsaru yogaŵa pakati pa Chipinda Chopatulika ndi Chipinda Chopatulikitsitsa ndi lotani?
-Nsaruyo imaŵakumbutsa a Isirayeli kuti ali osiyidwa ndi Mulungu chifukwa cha machimo awo.



34-Ndipo mtambo unaphimba chihema chokomanilana, ndipo ulemelero wa Ambuye unadzadza mkachisimo.

35-Ndipo Mose sanathe kuloŵa mchihema chokomanilanacho, chifukwa chakuti mtambo unakhalabe momwemo; ndipo ulemelero wa Ambuye unadzadza mkachisimo.

-A Isirayeli anakakhala kuti sanamange kachisiyo ngati m'mene Mulungu anaŵalamulililira, kodi ulemelero wa Mulungu unakabwera mkachisimo?
-Iyayi.

-Chifukwa chakuti A Isirayeli anamanga kachisiyo ngati m'mene Mulungu anaŵalamulililira, ulemelero wa Mulungu unabwera mkachisimo.

-Kodi a Isirayeli anakatha kuti adzipita kwa Mulungu mu njira yawoyawo?
-Iyayi.

-Kodi njira yokhayo, imene a Isirayeli anakamapitira kwa Mulungu inali yiti?
-Ya Mulungu Mwini.

-Kodi njira ya Mulungu tingayidziŵe bwanji?
-Kudzera M'buku la Mulungu, Bayibulo.

1-Ndipo Ambuye anamuwuza Mose kuti, “Dzisemere wekha magome aŵiri a miyala onga ngati oyamba aja, ndipo ndidzaremba pa magomewo mau amene anali pa magome oyamba, amene unawaswawo.
2-Ndipo ukonzekeretu maŵa m'maŵa, udzakwere m'phiri la Sinayi, ndipo udzayime pa maso panga pamwamba pa phiri.”

-Mose anamumvera Mulungu ndipo anasemanso mapale aŵiri a miyala napita nawonso ku phiri la Silayi.

-Ku phiri la Sinayi, Mulungu analembanso malamulo ake khumi aja pa mapale aŵiri a miyala, atsopano aja.

-Kodi mukukumbukira kuti Mulungu anamuwuza Mose kuti amumangire Iye Malo opatulika?

-Patapita nthaŵi, a Isirayeli anamanga Malo Opatulikawo ngati m'mene Mulungu anamulamulililila Mose.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 39:42-43 ndi 40:17

42-Chomcho a Isirayeli anayigwira ntchito yonse ngati m'mene Ambuye anamulamulilira Mose.
43-Ndipo Mose anayiwona ntchito yonseyo, ndipo anatsimikizara kuti anayigwira ngati m'mene Mulungu analamulililira.
17-Chomcho pa tsiku loyamba la mwezi oyamba, wa chaka chachiŵiri, kachisi anamangidwa.

-Chifukwa chakuti a Isirayeli anamanga Malo Opatulikawo ngati m'mene anaŵalamulililila iwowo Mulungu, ulemelero wa Mulungu unaloŵa M'malo Opatulikawo.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 40:34-35



15. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula mu Isirayeli kuti akafuna kupha nyama, adziyika dzanja lake pa mutu wa nyamayo?
-Mu Isirayeli ankayika dzanja lake pa mutu wa nyama imene ankafuna kuphayo, kuwonetsa kuvomereza pa maso pa Mulungu kuti iyeyo wachimwa ndipo akuyenera kufa, koma Mulungu wavomereza imfa ya nyama kuloŵa m'malo mwa munthuyo.

16. Kodi magazi a nyama anakatha kulipila pa machimo a a Isirayeli?
-Iyayi.

17. Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anaŵawuza a Isirayeli kuti adzipha nyama chifukwa cha machimo awo?
-Mulungu ankaŵaphunzitsa a Isirayeli kuti chilango cha tchimo ndi imfa.

18. Kodi ndani yekha,  amene amaloredwa kuloŵa ku Chipinda Chopatulikitsitsa chija?
-Aroni, wamkulu wamsembe.

19. Kodi wamkulu wamsembe amaloŵa  kangati ku Chipinda Chopatulikitsitsacho?
-Kamodzi pachaka pa tsiku limene amalisankha Mulungu.

20. Kodi Mulungu anamulamula Aroni kuti adzitenga chiyani, pa tsiku limene ankalisankha Mulungu kuti aloŵe Mchipinda Chopatulikitsitsacho?
-Mulungu anamulamula Aroni kuti adzitenga magazi a nyama poloŵa Mchipinda Chopatulikitsitsacho.

21. Kodi Mulungu ankachita chiyani, Aroni akapanga zimene Iye anamulamula, kuwaza magazi a nyama pamwamba pa chivundikiliro cha Likasa la Chipangano?
-Mulungu ankadikilira kaye osapereka msanga chilango

cha machimo awo kwa chaka chimodzi mpaka malipiro oy-
enera atachitika.

-Pamene Mose ankalankhulana ni Mulungu pamwamba pa phiri la Sinayi, kodi a Isirayeli ankachita chiyani pasi pa phirilo?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:1-6

1-Koma pamene anawona kuti Mose anachedwa kutsika m'phirimo, anthu anasonkhana kwa Aroni, nanena naye kuti, "Tipangireni milungu yakuti yidzititsogolera; Pakuti sitikudziŵa chimene chamuchitikira Mose amane anatitsogolera kuchokera m'dziko la Iguputo."
2-Ndipo Aroni anati, "Thyolani mphete za golide zimene ziri m'makutu a akazi anu, a ana anu amuna nda akazi, ndipo mubwere nazo kwa ine.
3-Ndipo anthu onse anathyola mphete za golide zimene zinali m'makutu mwawo, nabwera nazo kwa Aroni.
4-Ndipo Aroni anazilandira ku manja awo, nazisungunula, ndikupanga mwana wa ng'ombe pomuwenga mchikombole. Kenako anati, "Siyi milungu yanu, a Isirayeli, imene inakutulutsani inu m'dziko la Iguputo."
5-Aroni atachiwona chimenechi, anamanga guwa la msembe patsogolo pache; ndipo Aroni anafuwula kuti, "Maŵa alipo madyerero a Ambuye."
6-Ndipo maŵa lache, anthu anawuka m'mam'maŵa, nafukiza msembe yopsereza, nabwera nazo msembe za mgwirizano; ndipo anthu anakhala pansi ndi kudya ndi kumwa, nawukanso ndikuseŵera.

-Kodi a Isirayeli anachita chiyani pasi pa phiri la Sinayi?
-A Isirayeli anapanga mwana wa ng'ombe wa golide ndi kumampembedza.

-Kodi lamulo loyamba limene Mulungu analipereka kwa a



17-Ndipo Yoswa atamva phokoso la kupfuula kwa anthu, anati kwa Mose, "Kuli phokoso la nkhondo ku masakasa."
18-Koma Mose anati, "Phokosolo silikumveka ngati phokoso lopambana pa nkhondo kapena kulira kwa anthu olephera pa nkhondo. Ine ndikumva phokoso loyimba."
19-Mose ataŵandikira ku masakasa aja, ndikumuwona mwana wa ng'ombe wa golide uja ndipo anthu akuvina, anapsya mtima kwambiri. Ndipo anataya magome amene anali m'manja mwache, ndipo anaswekera mtsinde mwa phiri.

-Mose anaŵakwiyira a Isirayeli mwakuti anaponya pasi mapale a miyala a malamulo a Mulungu aja ndipo anasweka.

-Kodi kenako Mose anachita chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:20

20-Ndipo anatenga mwana wa ng'ombe amene anamupangayo, namutentha ndi moto ndikumpera mosalala, ndikumumwazira pa madzi. Ndipo Mose anaŵamwetsa ana a Isirayeli madziwo.

-Mose anayiwononga ng'ombe ya golide ija, ndipo anayipela, ndikutayila m'madzi ufa wakewo, kenako ndikuŵakakamiza a Isirayeli kuti amwe madziwo.

-Chifukwa chakuti Mose anaphwanya mapale a miyala, pamene Mulungu analembapo malamulo khumi aja, Mulungu anamuwuza Mose kuti asemenso mapale ena a miyala.

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 34:1-2

zidzukulu zanuzo, dziko lonse limene ndalilonjeza. Dziko limeneli lidzakhala lawo kwa zaka zonse.”

14-Ndipo Ambuye analeka kupereka chilango chimene amkafuna kuti aŵapatse anthu ache.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanaŵawononge a Isirayeli?
-Chifukwa chakuti Mose anapemphera kwa Mulungu kuti asaŵawononge a Isirayeli.

-Kodi Mose anamuwuza chiyani Mulungu kuti Iye asaŵawononge a Isirayeli?
-Mose anati kuti ngati Mulungu aŵawononge a Isirayeli, ndiye kuti a Iguputo adzanena kuti Iye anaŵatsogolera mchipululu ndi cholinga chafuna kuwapha.

-Mose ananenanso kuti, Mulungu anati kuti adzasunga lonjezo lake kwa Abulahamu, Isaki ndi Yakobo lakuti adzakhala ndi ana ambiri amene adzachuruke kwambiri.

-Chifukwa chakuti Mose anapemphera kwa Mulungu, Mulungu sanaŵawononge a Isirayeli.

-Kenako Mose anatsikanso mphiri la Sinayi lija.

-Kodi Mose anachita chiyani atatsikanso mphiri la Sinayi lija?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:15-19

15-Ndipo Mose anatembenuka natsika m’phirimo, magome aŵiri a Mboni ali m’dzanja lache; magome olembedwa ku mbali zonse ziŵiri.
16-Mulungu mwini ndi amene anapanga magomewo, ndipo analemba malamulowo mozokota pa magomewo.



Isirayeli linali lotani?
-Mulungu yekha ndiye oyenera kukhala Mulungu wa anthu onse.

-Kodi a Isirayeli amkatsogoza chinthu china chake patsogolo pa Mulungu?
-Inde.

-Kodi lamulo lachiŵiri limene Mulungu analipereka kwa a Isirayeli linali lotani?
-Munthu aliyense asapange fano kapena kulipembedza.

-Kodi a Isirayeli anapanga fano ndi kumalipembedza?
-Inde.

-Masiku apitawo, a Isirayeli anati kuti adzaŵamvera malamulo onse a Mlungu.
-Koma tsopano a Isirayeli ankaphwanya malamulo aŵiri oyamba amene Mulungu anapereka.

-A Isirayeli anaziwona zimene zimkachitika pa nthaŵi imene Mulungu ankatumiza milili kwa Farawo ndi a Iguputo aja.

-A Isirayeli anaziwona zimene zinachitika pa nthaŵi imene Mulungu anagaŵa madzi a Mnyanja Yofiira kuti iwowo awomboke.

-A Isirayeli anaziwona zimene zinachitika pa nthaŵi imene Mulungu anatumiza zimziri ndi mana kuchokera kumwamba.

-A Isirayeli anamuwona Mulungu akuŵapatsa iwowo madzi kuchokera mu tanthwe.

-Tsopano, a Isirayeli ankayipembedza ng’ombe ya golide,

ndipo ankalankhula kuti ng'ombe ya golideyo ndi imene inaŵatulutsa iwowo mu Iguputo.

-Kodi Mulungu anadziŵa kuti a Isirayeli ankapembedza ng'ombe ya golide?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:7-8

7-Ndipo Ambuye anati kwa Mose, Tsika mwamsanga mphiri muno, pakuti athu ako amene unaŵatsogolera poŵatulutsa mu Iguputo aja, adziwononga kwambiri.
8-Azisiya mwamsanga zonse zimene Ine ndanaŵalamula kuti azizichita zija. Adziyengera okha mwana wa ng'ombe wa golide, ndipo akumugwadira ndikumuphera msembe akunena kuti, “Iyi ndi milungu yanu imene inakutsogolerani pochoka m'dziko la Iguputo.

-Kodi Mulungu anadziŵa kuti a Isirayeli ankapembedza ng'ombe ya golide?
-Inde.

-Mulungu anaŵawona a Isirayeli pamene ankapembedza ng'ombe ya golide.
-Mulungu amawona zonse.

-Mulungu anamuwona Adamu ndi Eva pamene anadya chipatso chimene anaŵalamula kuti asadye.

-Mulungu anamuwona kayini akumupha Abele.

-Mulungu analiwona tchimo la anthu oyipa a ku Sodomu ndi Gomora.

-Mulungu anaŵawona abale ake a Yosefe akumugulitsa iye ngati kapolo ku Iguputo.



-Mulungu amaŵawona machimo onse ndiponso amadana ndi machimo onse.

-Kodi Mulungu anakwiya ndi a Isirayeli?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:9-10

9-Ndipo Ambuye anati kwa Mose, “Ndikuŵadziŵa anthu ameneŵa kuti ndi opulupudza.
10-Ndipo tsopano ndileke kuti ndiŵawononge, chifukwa chakuti ndili okwiya kwambiri koma iwe ukhala mtundu wawukuru wa anthu.”

-Mulungu anakwiya kwambiri ndi a Isirayeli.

-Mulungu anakwiya kwambiri ndi a Isirayeli mwakuti ankafuna kuti aŵawononge iwowo.

-Kodi Mose anati chiyani kwa Mulungu?

Tiyeni tiŵerenge Ekisodo 32:11-14

11-Ndipo Mose anapepha kwa Mulungu wache kuti, “Kodi Ambuye, mtima wanu upseranji pa anthu anu, amene munaŵaturutsa m'dziko la Iguputo ndi mphamvu yayikuru, ndi dzanja Lanu la mphamvu?
12-Kodi mukufuna kuti a Iguputo adzati, “Anaŵatulutsa a Isirayeli m'dziko la Iguputo ndi maganizo onyansa, ofuna kuti akaŵaphere ku mapiri ndikuŵawononga onse, kuti asawonekenso pa dziko la pansi? Ukali wanuwo Ambuye, oyaka ngati motowo, chonde muwutsitse, ndipo musaŵawononge anthu anu.
13-Kumbukirani Abulahamu, Isaki ndi Yakobo, atumiki anu, amene munaŵalumbilira ndikudzitchula nokha, amene munalankhula nawo kuti, “Ndidzachurukitsa mbewu zanu ngati nyenyezi za ku thambo. Ndidzazipatsa